

Danieli : 6:1-23

Mutu : Udindo wa Danieli pansi pa ulamuliro wa Dariyo

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero ndi tsiku labwino momwe Ambuye afuna tiyambe ndi mau apa Masalmo 34:19, amene akuti, “Masautso a wolungama mtima achuruka: koma Yehova amlanditsa mwa onsewa.”

Mupologalamu yatha tinali kusanthula Danieli 5:20-31 pamene timaunika tanthauzo la lembo, lolembedwa pakhoma. Ndipo lero pa Danieli 6:1-23, tikambirana za udindo wa Danieli pansi pa ulamuliro wa Dariyo.

Danieli 6

Ichi, ndichapterchozolowereka komanso chodziwika bwino, imene iri mbiri ya Danieli alim’dzenje la mikango.Tsono mwina tiyambe ndi funso lakuti, kodi mumadziwa kuti Danieli anapeza mtendere pamene anagonam’dzenje la mikangousiku uja, kusiyana momwe anakhala moyo wake wonse m’nyumba ya chifumu kuyambira pamene anali ndi zaka khumi ndi zisanu ndi ziwiri mpaka kufikira zaka makumi asanu ndi anayi?Tikunena kuti Danieli

anakhaliramphanthi kunyumba ya chifumu kusiya ndi kugonam'dzenje la mikango usiku umodzi.Ndikunena mau amenewa chifukwa chakuti pamene Danieli anagonam'dzenje la mikango, panalibe mkango ndi umodzi womwe umene unamukhutsa iye.Koma taonani kuti moyo wake unali pachiswe nthawi yonse pamene anali kukhala m'nyumba yachifumu, kuyambira Nebukadnezara, Nabonidusi, Belisazara ndi Dariyo mfumu ya Amedi ndiponso Koresi mfumu ya Aperesi. Koma ngakhale zinthu zinali chomwechi Danieli anali ndi mwayi wotsogolera anthu ena kwa Mulungu woonapamene anali kunyumba yachifumu.

Tsono tiyenera kusanthula moyo waDanieli m'dzenje la mikango usiku umodzi uja chifukwa ndiwo umene ukutikhudza kwambiri ife.Mbiri ya Danieli m'dzenje lamikangoikuonetsa mphamvu ya Mulungu ndi momwe Mulungu amatetezera ana ake komanso momwe adzatetezera ana ake m'nthawi yachibvuto chachikulu.Chapter chino ndi chapter 3, ndizogwirizana chifukwa ndi momwe tikuona Mulungu akulanditsa anyamata atatu, amene ndi anzake a Danieli mng'anjo yamoto. Tsono monga panali funso

lakuti, kodi Danieli anali kuti panthawi imene anzake aja anaponyedwamng'anjo yamoto, leronso funso lomwelo likuti, kodi anzake a Danieli anali kuti, pamene Danieli anaponyedwam'dzenje la mikango? Yankho likuti, sitikudziwa, koma tikunena kuti akanakhala kuti analipoakanalowa limodzi m'dzenje lija.

Wokondedwa anzanga apaulendo, chapter 3 ndi chapter 6 muli Uthenga wosunga anthu wokhulupirika a Israyeli ndi amitundu ina m'nthawi ya chibvuto chachikulu. Taonani m'chapter 3, tipezamo kuzunzika kwa wokhulupirira chifukwa cha udani wa anthu ndipo m'chapter 6, ndi momwe wokhulupirira akuzunzika ndi udani wa m'dierekezi. Pachifukwa chimenechi Uthenga kwa inu ndi ine lero lino ndi wakuti, “Khalaniodzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkangowobumaayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire” (1 Petro 5:8). Tere tikunenetsa kuti inu ndi ine, tikukhala dziko lino, lomwe ndi nkhwimba ya mkango (m'dierekezi), momwe ukubuma ndi kuyendayenda kufuna m'dani kuti umlikwire.

Tsono kudamkomera Dariyo kuika akalonga zana limodzi mphambu makumi awiri akhale m'madera onse a ufumu.

1. Ndi akuyang'aniraiwo akulu atatu, woyamba wawo ndi Danieli; kuti akalonga awa adziwerengere kwa iwo ndi kuti za mfumu zisasoweke.

Mundime ino tikuona kuti mutu wa golidi uja, kunena ufumu wa Babulo, wachotsedwa ndipo tsopano tiri ndi ufumu wa Amedi ndi Aperesi. Uwu, ndiwo ufumu uja wa manja mu loto la Nebukadneza. Mfumu Dariyo analamulira zaka ziwiri zokha, amene anatsagana ndi Koresi mwana wamlongo wake.

Tsono ngakhale talowa mu ufumu wina, koma tikuonabe Danieli alipaudindo wa nduna yaikulu pamene Dariyo akulamulamumuufumu wa Amedi. Ndiye ndifuna muone kuti monga loto la Nebukadnezara la fano lopangidwa ndi miyalayamtundu wosiyana-siyana, zikutanthauza kufookakwa ulamuliro wa muufumu. Tere, pano loto likukwanitsidwa chifukwa ufumu wa Nebukadnezara unali wamphamvu (autocratic), momwe sanagawane ulamuliro ndi wina aliyense. Koma muufumu uwu wa Dariyo, mulindunazokwanirazana limodzi ndi makumi awiri, amene anagawana udindo muufumuwu. Tsono mguluili, Dariyo anakhazikitsa anthu atatu amene anali amkhalapakati pa anthu

ndi mfumu, ndipo Danieli anali m'tsogoleri wa anthu atatuwa. Awa, anali ndi udindo wosungitsa chilungamo, mtendere ndi msonkho.

Tsono ndifuna muone kuti gulu la ndunali, ndilomwe likuimira atumiki a Mulungu kwa ife muulamuliro wake. Kutsindika kuti, inu ndi ine, tiri pansi paulamuliro wa mfumu ya pansi pano, komanso pansi paulamuliro wa atumiki a Mulungu. Iyi, ndiyo nkhani ili pa 1 Petro 2:13-14, pamene akuti, “Tadzigonjani kwa zoikika zonse za anthu, chifukwa cha Ambuye; ngakhale kwa mfumu, monga mutu wa onse; kapena kwa akazembe, monga otumidwa ndi iye kukalangaochita zoipa, koma kusimbaochita zabwino.”

2. Pamenepo Danieli amene anaposaakuluwa ndi akalonga, popeza munali Mzimu wopambana mwa iye, ndi mfumu inatiimuikewoyang'anira ufumu wonse.

Danieli anali mtsogoleri wandunazitatuzi, chifukwa anali wanzeru zopambana onsewa ndi wodzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu. Ndiye Pachifukwa chimenechi, tikuona kuti mfumu Dariyo adamuika Danieli kukhala wotsatira kwa iye. Tsono taonani kuti ngakhale Danieli anali wokalamba nthawi iyi (80 years), koma anali

wamphamvu mthupi ndi mumzimu momwe popeza anakangamirabe kuika chikhulupiriro chake mwa Mulungu woona.

3. Ndipo akuluwa ndi akalonga anayesa kumtola chifukwa Danieli, kunena za ufumuwo; koma sanakhoza kupeza chifukwa kapena cholakwira, popeza anali wokhulupirika; ndipo sanaona chosasamala kapena cholakwa chilichonse mwa iye.

Pano tiyeni tiyambe ndi mau akuti, pamene inu mukhala mtsogoleri m'mudzi, mumpingo ngakhaleenso pakayendetsedwekadziko, muyenera kudziwa kuti adani anu akukuyang'anani ndi diso la nsanje. Kunena kuti adani amakunenerani zoipa kapena kukuchitirani choipa pogwiritsa ntchito chofoka chiri chonse mwa inu.

Koma Danieli anali ndi moyo wochititsa chidwi, kotero kuti adani ake, sanathe kupeza cholakwa mwa iyeyu. Kutanthauza kuti inu ndi ine monga anthu wokhulupirira, tiyenera kukhala m'moyo umene zonse angatinenerezidzapezeka kuti ndi bodza.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikunena kuti inu simungathe kuletsa anthu kunena za inu, koma muyenera kukhala m'moyo umene udzawaonetsa poyera kuti ndiwo onama. Ichi, ndichimene Mtumwi Paulo kwa Afilipi 2:15, akulimbikitsa wokhulupirira kuti, “Kuti mukakhale wosalakwa ndi oona, ana a Mulungu opanda chirema pakati pa m'badwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko m'dziko lapansi.” Ndipo taonani Paulo mwini akudzichitira umboni pa Machitidwe Atumwi 24:16, pamene akuti, “M'menemonsondidziyesera ndekha ndikhala nacho nthawi zonse chikumbumtimachosanditsutsa cha kwa Mulungu ndi kwa anthu.” Kutsimikiza kuti Paulo sanali kutsutsika mumtima mwake pamene ayenda ngakhale kugona. Ndiye tikunenetsa kuti uwu, uyenera kukhala moyo wa inu ndi wanga ngati anthu wokhulupirira eni-eni. Kutsimikiza mau amkulu wina, amene anati chikumbumtima ndicho chinthu chimene chimasangalatsa munthu wamakhalidwe abwino. Kodi inu simusowa mtendere ndi chikumbumtima chanu?

4. Pamenepo anthu awa anati, sitidzamtola chifukwa chirichonse
Danieli amene, tikapandakumtola ichi pa chilamulo cha
Mulungu wake.

Danieli anali wosiyana ndi anthu ena ndipo Mulungu wake ndiye amene anapanga anthu amtundu wake kukhala wosiyana ndi ena. Taonani pamene anali mnyamataatangolowa kunyumba yamfumu, anasankha chakudya chamtundu wina. Tere kuyambira pamene paja, Danieli anali wosiyana ndi anthu ena onse, ndipo anthu enawonso analikudziwakusiyanaku pakati pawo. Ichi, ndichifukwa chake adani ake akunena kuti sangathe kupeza cholakwa mwa iye, pokha-pokha atagwiritsa ntchito lamulo la chipembedzo chake. Adani a Danieli amadziwa kuti anali wokhulupirika kwa Mulungu wake ndipo kuti anali kudalira pa Iye. Iwo anaona chimenechi chifukwa cha moyo wake wodalirapemphero. Ndiye adaniwa afuna autse mkangano pakati pa mfumu ndi chipembedzo cha Danieli.

5. Ndipo akuru awa ndi akalonga anasonkhanakwa mfumu mofulumira, natero nayo mfumu Dariyo, mukhale ndi moyo chikhalire.

6. Akuru onse a ufumuwo, ndi akazembe ndi akalonga, mandoda, ndi ziwanga, anapanganakukhazika lemba lachifumu, ndi kuikapocholetsacholimba kuti ali yense akapempha kanthu kwa mulungu aliyensekapena kwa munthu ali yense, masiku makumi atatu, osati kwa inu nokha, mfumu, adzaponyedwam'dzenje la mikango.

Pano akuru onse, apangana chiwembu chomwe akuchita mochenjera kwambiri. Ndikoyenera pano kunena kuti mfumu Dariyo anali munthu wabwino, koma anali ndichofoka chakuti anamvomerezachinyengo chomwe chinakonzedwa.

Lero lino m'mipingoyathuyi muli bvuto limeneli pakati pa akristu, makaiwo amene ali ndi chuma chochuluka, amene m'tsogoleriamachitanawomwachinyengopowalemekeza. Nkhani ikuti inu ngati mtsogoleri, simuyenera kuchita mwachinyengo ndi cholinga chakuti mupezethandizo la chuma ayi. Tikunena kuti inu ndi ine, tiyenera kusamala chifukwa anthu ambiri adzanena kuti ziribwino pamene akunena zabodza.

Ndikunena mau onsewa chifukwa akuru ndi nduna zonse zinanamiza mfumu Dariyo, amene amamvera zonena zawo. Tsono

mwa mau achinyengo amenewa, mfumu Dariyo anafika podziika pamwamba ngati mulungu,kotero kuti mapemphero amaperekedwakwa iye.

7. Tsopano mfumu mukhazikitsecholetsacho, ndi kutsimikiza cholembedwacho, kuti chisasinthike monga mwa malamulo a Amedi ndi Aperisi, amene sasinthika.

8. Momwemo mfumu Dariyo anatsimikizacholembdwa ndi choletsacho.

Pano mfumu Dariyo akuonetsa kufookakwa moyo wake chifukwa akukhazikitsacholetsacho ndi kutsimikiza cholembedwacho- lamulo Amedi ndi Aperisi. Tsono pamene mfumu yasainira, zikutanthauza kuti palibe amene angasinthe ngakhale mfumu imene.Zonsezi zikukonzedwa ndi cholinga chofuna kupeza Danieli cholakwa.

9. Ndipo podziwa Danieli kuti adatsimikizacholembdwa, analowa m'nyumba mwake, m'chipinda mwake, chimene mazenera ake anatsegukaoloza ku Yerusalemu; ndipo anagwadamaondo ake tsiku limodzi katatu, napemphera, nabvomereza pamaso pa Mulungu wake monga umo amachitira kale lonse.

Tsopano lamulo la sainidwa, lomwe likhozakumuikaDanieli m'mabvuto, koma sadapitekwa mfumu kukadandaula kapena kuyesa kuchotsetsa ayi, popeza amadziwa kuti ndichinthu chosathekakusinthidwa. Tere, Danieli anangopita kukapemphera monga mwanthawi yonse m'nyumba mwake kuloza ku Yerusalemu. Kutanthauza kuti moyo wa Danieli unali kuona ku Yerusalemu komwe kunali Kachisi wa Mulungu wake, kotero kuti sanasinthe chifukwa cha lamulo ili ayi. Tsono ife lero, sitienera kukhala ndi malo amene tikhoza kuwakhulupirirakuperekako mapemphero athu ayi, koma kwa Ambuye wathu Yesu Kristu basi. Ichi, ndichimene Ambuye Yesu pa Yohane 4:21, 24, adanena kuti, "Tamvera Ine, mkazi iwe, kuti ikudza nthawi imene simudzalambira Atate kapena m'phiri ili, kapena m'Yerusalemu.Mulungu ndiye Mzimu ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mu Mzimu ndi m'choonadi."

Nkhani ikunena kuti Danieli sanasiye kupembedzaMulungu wake komanso kutumikira mfumu ngakhale anadziwa kuti lamulo linakhazikitsidwa chifukwa cha iye. Kutsimikiza kuti inu ndi ine,

sitiyenera kusiya kupembedza kapena kutumikira Mulungu chifukwa choopakuzunzidwa ayi.

Ndiye pamene tiwerenga verse 11-15, tikumva kuti adani a Danieli anadziwa kuti Danieli sangapembedzemulungu wina, kotero kuti tsopano apita kwa mfumu Dariyo kukamuuza kuti Danieli waphwanya lamulo lomwe mfumuyoanasiiyila. Mwachisoni kuti mfumu Dariyo sakanathakusinthamulo pa iye yekha koma akanakhala Nebukadnezara akanakhoza chifukwa lamulo linali m'manja mwa iye yekha. Uku ndiko kufookakwa ulamuliro wa democracy. Tere pano palibe chimene mfumu angachite kotero kuti Danieli ayenera kuponyedwam'dzenje la mikango.

10. Pamenepo anasonkhana anthu awa, napeza Danieli alikupemphera ndi kupembedza pamaso pa Mulungu wake.

16. Pamenepo inalamula mfumu, ndipo anadza naye Danieli, namponyam'dzenje la mikango. Ndipo mfumu inalankhula, nitikwa Danieli, Mulungu wako amene umtumikira kosalekeza, Iyeyu adzakulanditsa.

Pano ndifuna tigwire mau akuti, "Mulungu wako amene umtumikira kosalekeza, Iyeyu adzakulanditsa." Ndime iyi,

ikutionetsa kuti akunja nawo anali kukhulupirira kuti milungu ikhoza kulanditsa wopembedza awo.Tere ndichifukwa chake tikuona kuti Dariyo anazindikira mulungu, koma osati kudziwa anali kudziwa Mulungu weni-weni ayi. Taonani iye analikudziwa momwe Mulunguyo anapulumutsira anyamata atatu aja mu Danieli 3:26-27. Mfumu Dariyo pano ali ndi chikhulupiriro chakuti Danieli aturutsidwa, ngakhale iye akanakondakumuturutsa koma analibe mphamvu zimenezi. Kutsimikiza kuti mafumu ndiwo anthu amene amakondwerakumvera anthu amene amawanamiza.Koma tikuphunzira kuti anthu onse amakhumbira chilungamo cha Mulungu chomwe chimaonekera mwa anthu ena, koma samafuna kukhulupirira Mulunguyo.

17.Ndipo anatenga mwala, nauika pakamwa pa dzenje, niukomera mfumu ndi chosindikizira chake ndi chosindikizira cha akuru ake, kuti kasasinthike kanthu ka Danieli.

Mfumu Dariyo waonererakutsekeredwakwa Danieli ndi mwala pakamwa padzenje la mikango. Danieli anagona usiku wonse m'dzenje la mikango.Ndiye tiyenera kudziwa kuti mikango iyi, inali

yoopsa,yolusayakutchire ndipo sitiyenera kunena kuti inalibe mano ayi.Tere awa, anali malo abwino ndi wotetezeka bwino, momwe Danieli anagonaturotabwino, kusiyana ndi mfumu Dariyoamene anabwerera kunyumba kwake, atasauka kwambiri chifukwa cha Danieli kotero kuti sanathe kudya komansosanagone usiku onse. Ichi, chinali chinthu chochititsa chidwi kuti munthu amene anali m'dzenje la mikango ndiye anapeza mtendere kusiyana ndi amene anagona m'nyumba yachifumu.Kutsimikiza mau akuti choipa chitsata mwini.

19.Nilawirira mamawa mfumu, nimuka mofulumira ku dzenje la mikango.

20.Ndipo poyandikirapadzenjeinapfuula ndi mau achisoni mfumu, ninena, nitikwa Danieli, Danieli, mnyamata wa Mulungu wamoyo, kodi Mulungu wako, amene umtumikira kosalekeza, wakhozakukulanditsa kwa mikango?

21.Pamenepo Danieli anati kwa mfumu, Mfumu, mukhale ndi moyo chikhalire.

22.Mulungu wanga watumamthenga wake, natseka pakamwa pa mikango; ndipo siinandipweteka, chifukwa

anandionawosachimwa pamaso pake, pamaso panunso mfumu, sindinalakwa.

Pano mfumu ikufunsa ngati Mulungu wa Danieli anakhoza kumulanditsa kwa mikango. Tsono sizikudziwika ngati Dariyo anali kuyembekeza yankho kuchokera kwa Danieli. Koma taonani Danieli akuyankha mwaulemu ndi kumulonjera mwaulemu monga anali kuchitira nthawi zonse pomufunira moyo wautali. Ndiye taonani Danieli analandira mthengawa Yehova, monga yemwe uja anyamata anzake analandira mng'anjo yamoto. Uyu, ndiye uja tidanena kuti anali Ambuye Yesu Kristu asanabvale thupi la munthu, amene mfumu Nebukadnezara adaona mng'anjo yamoto.

23. Pamenepo mfumu inakondwera kwambiri, niwauzaaturutse Danieli m'dzenje. Momwemo anamturutsa Danieli m'dzenje ndi pathupi pake sipadaoneka bala, popeza anakhulupirira Mulungu wake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, mfumu Dariyo anamukonda Danieli, kotero kuti pamene adamuona wamoyo anakondwera kwambiri. Ndiye tikutsindika kunena kuti Danieli anapulumutsidwa mwachikhulupiro chake mwa Mulungu

wake. Kutsimikiza mau aja analembedwa pa Ahebri 11:33, pamene anati, “Amene mwachikhulupiro anagonjetsa maufumu, anachita chilungamo, analandira malonjezano, anatseka pakamwa mikango.” Ichi ndicho chikhulupiro chopulumutsa. Kodi inu, mudachilawa kale chipulumutso chimenechi?

Lero tilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula Danieli 6:1-23, momwe timakambirana za udindo wa Danieli pansi pa ulamuliro wa Dariyo.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!